Kufunika kwa kusunga mbeu yamaonekedwe abwino

Anthu akatha kukolola, ngati mbeu sizinasamaliridwe bwino, zitha kusakazika (kudyedwa ndi tizilombo, kusakazika ndi chinyontho, ndi zina zotero…).

Ndi kwabwino kwambiri kutsata njira zoyenerera zosungira mbeu. Njira zimenezi zifunika kusunga mbeu zonse zimene zabwezedwe moyenera kuti muzakhale ndi mbeu yabwino yozabzala chaka china.

Musanasunge:

1- Mbeu ziyanikidwe mukatha kukolola kuti zisachite chuku.

2- Chikakhala chimanga, sankhani mikuta ikuluikula yabwino. Chimanga chokhacho cha pakati pa chitsononkho (chitsontho) chisungidwe ngati mbeu.



3- Kusankhira: mbeu yabwino yokha ndi yomwe ingabzalidwe: yonse yofumbwa, yosweka, yosaoneka bwino, mphwepwa ndi yowola ichotsedwe.

4- Polewa kuti mbeu zisaonongedwe ndi tizilombo (makamaka chimanga), ziyenera kuthiridwa mankhwala

- Kuteteza kwa chilengedwe: Ombwe kapena Nimu
- Kuteteza ndi mankhwala: Akiteliki

This document has been produced with the financial assistance of the European Union. The contents of this document are the sole responsibility of Inter Aide and can under no circumstances be regarded as reflecting the position of the European Union.

Mukasunga:

1- Mbeu zisungidwe malo otetezedwa, otsekedwa ndi loko kuteteza umbava.

2- Nkhokwe ikhale yosamalirika ndi mkati mukhale mowala pofuna kulewa chinyontho.

3- Matumba ayalidwe pa thandala pa theka ya mita imodzi kuchoka ku khoma pofuna kulewa chinyontho.



Phulutsa, mchenga ung'onoung'ono kapena fumbi ziikidwe pakati pa matumba pofuna kuchepetsa kuti mbeu zisaonongedwe ndi tizilombo.

4- Polewa kuti mbeu zisaonongedwe ndi makoswe gwiritsani ntchito mankhwala, zigwenembe ndi mphaka.



Inter Aide
Agro Phalombe Project
PO Box 318
Zomba - Malawi

Kukhala ndi nkhokwe yosungiramo mbeu m'mudzi mwanu

CHICHEWA

November 2009

Laurence Mathieu-Colas
Goulven Le Bahers
Translation : Mr. Laston M. Makina

http://www.interaide.org/pratiques

Kodi nkhokwe yosungiramo mbeu n'chiani?

Nkhokwe yosungiramo mbeu ndi mbeu yonse yomwe yasonkhanitsidwa malo amodzi ndi gulu (mudzi, magulu a zaulimi).

Cholinga cha nkhokwe yosungiramo mbeu ndi:

1- Kupeza mbeu zotsiyanatsiyana za makono

2- Kupeza mbeu pangongole ndi kusavutikira mbeu m'nyengo yobzala

Cholinga chotsiriza ndi kuchulukitsa zokolola:

☞ Chakudya: kulimbana ndi njala



☞ Kugulitsa: Kuchulukutsa chuma ndi kupititsa patsogolo m'yoyo yathu

Kodi zimayenda bwanji?

Mbeu zimasungidwa pagulu.

M'nyengo yobzala, munthu yemwe ali mgululi amatenga mbeu pangongole kuchokera ku malo osungiramo mbeu.

Anthu akatha kukolola, ali yense amabwezera ku nkhokwe yosungiramo mbeu yochuluka kawiri pa mbeu yomwe analandira.

Mbeuzo zimasungidwa m'malo osamalirika mpaka kufika m'nyengo yina. Ndipo zimagawidwanso kwa anthu a m'gulumo.

Ngati gulu lingapitirize kuchita izi chaka chiri chonse, mbeu zizichulukirachulukira m'nkhokwe yosungiramo. Gulu lizakhala ndi mbeu chaka chiri chonse.



Kodi gulu lingatani ngati mbeu itachuluka?

1- Munthu aliyense apeza ngongole ya mbeu yochuluka.

2- Anthu ena azalandiridwa kuti nawonso apindule pakutenga ngongole ya mbeu.

3- Gawo lina la mbeu litha kusungidwa kuti ngati kubweza kungazavute chifukwa chakusakolola bwino, mbeu isasowe.

4- Gawo lina la mbeu litha kugulitsidwa.



Ndalamazo zitha kugwiritsidwa ntchito:

- kugulira mbeu ya chimanga pa zaka zitatu ziri zonse (mbeu ya masika)
- kugula mankhwala (akiteliki, feteleza...)
- zifukwa zina zomwe gulu lingafune kuchita